**TSIKU LA MAPEMPHERO A PA DZIKO LA PANSI LOPEMPHERERA KUITANIDWA – LA MULUNGU LA KUITANIDWA, 2018**

**UTHENGA WA APAPA FRANCIS**

**MUTU**: ***KUMVETSERA, KUSINKHASINKHA NDI KUKHALA MOYO WOITANIDWA MWA AMBUYE***

**Okondeka Abale ndi Alongo**

Mwezi wa October ukubwerawu, ku Msonkhano Waukulu wa ma Bishop wa Sinodi wa nambal 15, adzakumana ndi kukambirana za mutu wa achinyamata, makamaka za ubale wa pakati pa achinyamata, chikhulupiriro ndi kuitanidwa. Kumeneko tidzakhala ndi mpata woganizira mozama kwambiri za mmene pakati pa moyo wathu pali kuitanidwa ku chimwemwe chomwe Mulungu akutiuza ndi momwe izi zili, "Dongosolo la Mulungu pa amuna ndi akazi pa nthawi zonse." (Sinodi ya ma Bishop, Msonkhano wa Ukulu wa nambala 15 – Achinyamata, Chikhulupiriro Ndi Kusinkhasinkha Za Kuitanidwa. *Mau Oyambirira*).

Msonkhano wa nambala 55 wa Tsiku La Mapemphero A Pa Dziko Lapansi Lopempherera Kuitanidwa, ulalikanso Uthenga Wabwino kwa ife, momveka bwino kwambiri. Sindife anthu onzunzika chifukwa zinayera kutero kapena ongotengeka ndi zochitika zosalumikizana ayi: Pa mbali ina, moyo wathu ndi kukhala kwathu mu dziko lino la pansi ndi zipatso za kuitanidwa ku umulungu! Ngakhale pakati pa nthawi ino yovuta, misteri ya kusanduka munthu kwa Mulungu Mwana imatikumbutsa kuti Mulungu nthawi zonse amabwera kuti akumane nafe. Ndi Mulungu ali nafe, amene amayenda nafe kawirikawiri pa miseu ya fumbi ya moyo wathu. Amadziwa nkhawa zathu zofuna chikondi ndipo amatiyitana ku chikondwerero. Mkuchuluka kwa kuitanidwa komanso mkusiyana kwa kuitanidwa kuli konse, payekha kapena ku Mpingo, pamafunika kumvetsera, kusinkhasinkha ndi kukhala mu mau amene amatiyitana kuchokera kumwamba ndipo pamene akutithandiza kupititsa pa tsogolo luso/mphatso zathu, mauwa amatipanga ife kukhala zida za chipulumutso pa dziko la pansi pano ndipo amatiperekeza ku chimwemwe chathunthu.

Zinthu zitatu izi: Kumvetsera, Kusinkhasinkha ndi Kukhala – zinaliponso pa chiyambi cha ntchito yake Yesu, pamene, atamaliza nthawi yake yopemphera ndi kulimbana ndi satana mu mchipululu muja, adapita ku nyumba ya Mapemphero ku Nazarete. Kumeneko adamvetsera Mau a Mulungu, adasinkhasinkha za ntchito imene adapatsidwa ndi Atate ake, ndipo adalengeza kuti adabwera kudzayikwaniritsa,"Lero." (Lk. 4: 16 – 21).

**Kumvetsera**

Kuitana kwa Ambuye – tineneratu kuyambira pa chiyambi – sikuoneka bwinobwino ngati zinthu zimene titha kumva, kuona kapena kugwira pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Mulungu amabwera mwakachetechete ndi mosaoneka, mosatiphwanyira ufulu wathu. Zimatha kuchitika kuti Mau ake samveka chifukwa cha nkhawa zambirimbiri ndi madandaulo amene amadzadza mmaganizo ndi mmitima mwathu.

Tikusoweka tsono kuphunzira kumvetsera mosamala Mau ake ndi mbiri ya moyo wake, komanso kuti tikhale tcheru kuzochitika za moyo wathu wa tsiku ndi tsiku, kuti tiphunzire kuona zinthu ndi maso achikhulupiriro, ndikuti tithe kukhala otsekuka ku zodabwitsa za mzimu.

Sitidzatha kuzindikira mwapadera kuitanidwa kwathu komwe Mulungu alinako mu mtima mwake, ngati tikhala osatsekuka mwa ife tokha, mu njira yathu yochitira zinthu yosakhazikika, mwa iwo amene alibe chidwi ndipo amakhala mkati mwa kadziko kao kang'ono.

Titha kutaya mwai wolota zazikulu woti titenga nao mbali mu mbiri ya padera ndi ya pachiyambi yomwe Mulungu akufuna kuyilemba ndi ifeyo.

Yesu nayenso adayitanidwa ndi kutumidwa. Ichi ndi chifukwa chake adayenera kuyamba wadzikonzekera mwakachetechete pa yekha. Adamvetsera ndi kuwerenga Mau a Mulungu mu nyumba ya mapemphero, ndi kuwala ndi mphamvu za Mzimu Woyera, adaulula tanthauzo lenileni la Mauwo, podzilozera iye mwini ndi mbiri ya mtundu wa Israel. Masiku ano kumvetsera kukukhala kovuta kwambiri, tiri kukhala pakati pa anthu odzadzidwa ndi phokoso, amene amatengeka kwambiri ndi kulandira mauthenga osiyanasiyana mowirikiza. Phokoso la kunja lomwe nthawi zina liri mmizinda yathu ndi malo oyandikana nao kawirikawiri limatsagana ndi mkati mwathu momwe muli mosakhazikika komanso chipwirikiti. Izi zimatilepheretsa kuti tikhale chete kaye ndi kuti tilawe kukoma kosinkhasinkha, kuganizira modekha pa zochitika zonse za mmoyo wathu, kugwira ntchito zathu ndi chikhulupiriro cha chikondi cha Mulungu mundondomeko yake ndi kusankha moyenerera.

Monga tikudziwa, Ufumu wa Mulungu umadza mwakachetechete komanso mosadziumiriza okha (Lk 17:21) ndipo titha kusonkhanitsa njere zake monga mneneri Elia. Timalowa mkatikati mwa mzimu wathu ndipo timakhala otsekuka kukunong'ona kosamveka kwa kamphepo ka umulungu (1 Mafumu 19: 11 – 13).

**Kusinkhasinkha**

Pamene Yesu, ku nyumba ya Mulungu ku Nazarete, akuwerenga mau a mneneri Yesaya, akusinkhasinkha za gawo la ntchito yomwe adatumidwa ndipo akuipereka kwa amene amayembekezera Mpulumutsi: Mzimu wa Ambuye uli pa ine, chifukwa wandidzoza kuti ndikalalikire amphawi Uthenga Wabwino. Wanditumа kuti ndikalengeze kwa am'ndende kuti adzamasulidwa ndi kwa akhungu kuti adzapenyanso. Wanditumа kuti ndikawapatse ufulu anthu osautsidwa, ndi kulalika za nthawi imene Ambuye adzapulumutsa anthu ao" (Lk 4: 18 – 19).

Motero, aliyense wa ife angathe kuzindikira payekha kuitanidwa kwake podzera nkusinkhasinkha mwa uzimu. Iyi ndi "ndondomeko yomwe munthu payekha amapanga chisankho chofunikira kwambiri, mokambirana ndi Ambuye ndi kumvetsera mau a Mzimu Woyera, kuyambira posankha moyo womwe akufuna kutsata." (SINODI YA MABISHOP, MSONKHANO WA UKULU WA NUMBALA 15. Achinyamata, Chikhulupiriro ndi Kusinkhasinkha Za Kuitanidwa. II. 2).

Apa ndi pamene timazindikira kuti kuitanidwa kwa Chikhristu kuli ndi mbali ina ya uneneri. Mau a Mulungu amatiuza kuti aneneri onse amatumidwa kwa anthu pa nthawi yovuta kwambiri monga pamene chitetezo palibe pa nkhani ya katundu, moyo wa uzimu ndi pamene chikhalidwe chosokonezeka, kuti mdzina la Mulungu apereke uthenga wotembenuza mtima, chiyembekezo ndi wothunzitsa mtima. Ngati mphepo ya kavulumvulu, mneneri amatsutsa nthumanzi ya mtendere wa bodza yomwe idayiwala Mau a Chauta. Amasinkhasinkha zochitika mounikiridwa ndi lonjezo la Mulungu ndipo amathandiza anthu kuti aone zizindikiro za mbandakucha pakati pa mdima wa mbiri yao.

Leronso, tikusowa kusinkhasinkha kwakukulu ndi kwa uneneri. Tiyenera kulimbana ndi zinyengo za maganizo olakwika ndi maganizo otsutsa nthawi zonse, ndi kuzindikira, mu ubale wathu ndi Ambuye, malo, njira ndi nthawi zimene amatiyitanira. Mkhristu aliyense ayenera kukula kuti athe "kudziwa mwa iye yekha" moyo wake ndi kumvetsa komwe akuitanidwira kapena chomwe akuitanidwira ndi Ambuye, kuti athe kugwira ntchito yake.

**Kukhala**

Pomaliza, Yesu akulengeza kwatsopano kwa nthawi ino, imene idzadabwitsa ambiri ndi kuumitsa mitima ya anthu ena. Nthawi yakwana ndipo iye ndiye Mpulumutsi wolonjezedwa amene mneneri Yesaya adamulengeza, wodzozedwa kuti apereke ufulu kwa am'ndende, kuti akhungu apenyenso ndi kulalikira za chifundo cha Mulungu cha chikondi kwa cholengedwa chiri chonse. Zoonadi, Yesu akuti, "Lero zachitikadi zimene adaaneneratu Malembo amene mwamvawa." (Lk 4: 21).

Chimwemwe cha Uthenga Wabwino, chimene chimatipangitsa kukhala otsekuka kukumana ndi Mulungu, abale ndi alongo athu, sigwirizana ndi kuchedwa/kuzengereza ndi kukhala ulesi. Chimwemwe cha Uthenga Wabwinochi sichingadzadze mitima yathu ngati tikhala ozengereza chifukwa choganiza kuti nthawi yayenera siinafike, koma kuli kanana lero chifukwa choopa kupanga chisankho. Kuitanidwa ndi lero! Utumiki wa Chikhristu ndi leronso ! Aliyense akuitanidwa: kaya ndi ku moyo wa banja, unsembe kapena ku moyo wodzipereka mwapadera – ndi cholinga choti tikhale mboni za Ambuye lero osati mawa.

Tsiku limene Yesu adalilengeza limatitsimikizira kuti Mulungu amapitiriza "bwera" kuti apulumutse mtundu wa anthu ndi kutipanga ife kukhala ogawana naye ntchito yake. Ambuye akupitiriza kuitana anthu ena kuti akhale naye ndi kumutsatira mwa ubale weniweni. Akupitiriza kuitana ena kuti amutumikire moonekera. Ngati atilola kuzindikira kuti akutiyitana kuti tidzipereke tokha kwathunthu ku ufumu wake, apo tisakhale ndi mantha! Ndi zabwino – ndipo ndi chaulere chachikulu – kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu ndi kuutumiki wa abale ndi alongo athu.

Lero Ambuye akupitiriza kuitana ena kuti amutsate. Tisayembekezere kuti tikhale opanda banga kuti tiyankhe kuti "inde" ndi mtima wonse, tisakhale ndi mantha chifukwa cha zofooka ndi machimo athu, mmalo mwake titsekule mitima yathu ku mau Ambuye. Kumvera mauwo, kusinkhasinkha utumiki wathu mu Mpingo ndi mdziko la pansi, ndiponso kukhala moyo otumikira umene Mulungu amatipatsa masiku onse.

Maria Woyerawoyera, yemwe anali namwali odzichepetsa, adaamva, adavomera ndipo adakumana ndi Mau a Mulungu odzipanga munthu; iye yemwe atiteteze ndi kutiperekeza nthawi zonse pa ulendo wathu.

***Kuchokera kuVatican, 3rd December, 2017 - Lamulungu Loyamba La Advent***

**Apapa Francis**